Yesetsani Kuti Muzilambira Mulungu M’njira Yovomerezeka (Gawo 2)

Nkhaniyi yachokera m’mutu 16 m’buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* Bukuli likupezekanso pawebusaiti ya jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso chifukwa chake mumazikhulupirira. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa kenako onani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI AKHRISTU OONA AYENERA KUMAUZA ENA ZIMENE AMAKHULUPIRIRA?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N’chifukwa chiyani anthu ena anganene kuti inde?

N’chifukwa chiyani ena anganene kuti ayi?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

N’chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Akhristu oona amapewa kukangana ndi anthu pa nkhani zimene anthuwo amakhulupirira.
(Werengani mutu 16 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 13-17.)

Werengani Akolose 4:6.
Kodi vesili likusonyeza bwanji kuti tiyenera kukhala osamala tikamafotokozera ena zimene timakhulupirira?

Werengani Mateyu 7:12.
Ngati ena sakugwirizana ndi zimene timakhulupirira, n'chifukwa chiyani tiyenera kuwalemekezabe?



Tikamaponyera mnzathu mpira, timauponya m'njira yoti asavutike kuwakha. Mofananamo, tiyenera kufotokozera ena zimene timakhulupirira mosamala komanso mwaulemu

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Akhristu oona amasonkhana pamodzi kuti aphunzire mmene angafotokozere zimene amakhulupirira kwa ena.

(Werengani mutu 16 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 18-19.)

Werengani Salimo 22:22; Aroma 1:12 ndi Aheberi 10:24, 25.

Kodi timapindula bwanji tikamasonkhana ndi Akhristu anzathu polambira Mulungu?

Werengani Malaki 3:10.

Kodi timapindula bwanji tikamayesetsa kulambira Mulungu m'njira yovomerezeka?

Kodi **inuyo** mungauzeko ndani zimene mumakhulupirira, ndipo mungachite bwanji zimenezi?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

NGATI WINA ATANENA KUTI…

Nthawi zonse a Mboni za Yehova amakakamiza anthu ena kuti azitsatira zimene iwowo amakhulupirira.

MUNGAYANKHE KUTI…

N'zoona kuti timakonda *kuuza* ena zimene timakhulupirira koma *sitimawakakamiza* kuti asiye zimene amakhulupirira chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Poganizira zimene munthuyo wanena, kodi mungamuthandize bwanji pogwiritsa ntchito mfundo za palembali?

_____

NGATI WINA ATANENA KUTI…

Chipembedzo sasankhirana, ndiye palibe chifukwa choti anthu azikambirana zimene amakhulupirira.

MUNGAYANKHE KUTI…

Anthu ambiri masiku ano amaganizadi choncho. Koma Baibulo limatilimbikitsa kuti tizikambirana zimene timakhulupirira chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge naye lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Poganizira zimene munthuyo wanena, kodi mungamuthandize bwanji pogwiritsa ntchito mfundo za palembali?

_____

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania